

# SATANA WALEPHERA KATATU KONSE KUTI ALANDE MALO A MULUNGU

**Yolembedwa ndi Tony Alamo**

Kodi simumadandaula mukaganizira zoti Satana wanyenga dziko lonse? Iye wakhala, katatu konse, akuyesapo mowonetsera kuti atenge malo a MULUNGU ndiponiso kuti ahotse ufumu wa MULUNGU kuti aikepo ufumu wake. Kawiri konse Satana walephereratu mochititsa manyazi, ndipo panopa akuyesetsabe kwa nthawi yachitatu ndipo kuyesera kumeneku kumene kukuchitika paola linoli posachedwapa kulepherekanso.

Nthawi yoyamba imene Satana anayesa kulanda malo a MULUNGU inali M'munda wa Edene, pamene Satana anafunsa Hava kuti, "Ndipo anatitu Mulungu?" Genesis 3:1-3 amati, "Ndipo njoka [Satana] inali yakuchenjera yoposa zamoyo zonse za m'thengo zimene anazipanga YEHOVA MULUNGU. Ndipo inati kwa mkaziyo, Ea! ndipo anatitu MULUNGU, Usadye mitengo yonse ya m'mundamu? Ndipo mkazi [m'malo moyidzudzula ndi kuyikana] anati kwa njoka, tikhonza kudya zipatso za mitengo ya m'mundamu." Koma MULUNGU anati, za chipatso cha mtengo wapakatikati pa munda, "Musadye umenewo, musakhudze umenewo, mungadzafe." Pamene MULUNGU ananena kuti "mungadzafe," IYE sankatanthauza kuti imfa ndi chinthu cha kanthawi kochepta chabe. IYE ankatanthauza kuti imfa ndi imfa yamuyaya kwa mwamuna kapena mkazi, yosatha mumalawi a moto a Gehena, imfa yopanda chikiriro. Mfundu za zimenezi zikupezeza



*Abusa Tony ndi Susan Alamo pamodzi ndi gulu loimba papulogalamu ya pa TV yooneka dziko lonse chithunzi chinajambulidwa 1974*

mu Malemba a Chipangano Chakale ndi Chipangano Chatsopano chomwe.<sup>1</sup>

Mkaziyo, komanso anthu ambiri masiku ano padziko lapansili, sankadziwa kuti munthu akamvera Satana, amakhala akuvomoreza kuti akumane ndi mavuto oopsa kwa tuyaya, gehena wosatha, amene asowetsa mtendere kotheratu kumzimu komanso kumaganizo a anthu ake. Utsi udzatuluka kuchoka m'matupi a anthu amene akuwotchedwa ku Gehena kosalekeza (Chivumbulutso 14:9-11). Anthu amene amalambira (monga kuchita zofuna za) Satana, boma lake limodzi, ndiponiso tchalitchi chake chadzikolo lonse (Katolika) nawonso adzaona zakuda ku Gehena.<sup>2</sup> Satana mowoneka ngati njoka, ndi kuchenjera kwake, ananyenga Hava, ndipo panopa akunyenga dziko lonse lapansi.<sup>3</sup>

Mu Chivumbulutso 12:9, Satana akutchedwa kuti ndi chinjoka chachikulu.

"Ndipo chinaponyedwa pansi chinjoka chachikulu [kuchoka Kumwamba], njoka yokalambayo, iye wotchedwa mdierekezi, ndi Satana, wonyenga wa dziko lonse." Satana ankadziwa kuti akangonyenga Hava, ndiye kuti dziko lonse likhala m'manja mwake.<sup>4</sup> Choncho Hava anakhala mtumiki woyambirira wa Satana; anakhala mbuzi yoyamba. Ngati munthu akufuna kukhala mbuzi ya Satana, ndiye kuti sungakhulupirire YESU, kapena kukhala m'modzi mwa ophunzira AKE. Sungakhale moyo wa njira ya mtanda ya KRISTU, koma nkumachita chilichonse chimene ukufuna. Sungakhale mboni ya KRISTU koma nkumamukana IYE, IYE amene anabwera padziko lapansi kudzapulumsa anthu ochimwa.<sup>5</sup>

Pamene Satana anaauza Hava kuti iwe sudzafayi, koma udzafanana ndi MULUNGU, moti idya chipatsochi ndipo chomwecho upatseko mwamuna wako, Hava anamveradi Satana, ndipo anamukopa mwamuna wake. Maso awo anatseguka (Genesis 3:7). Iwo anadziwa kuti achimwa ndiponiso kuti ananamizidwa. Kungoyambira pamenebo Satana ndi amene wakhala akulamulira dzikoli m'malo mwa iwovo, ndipo panalibe chilichonse kupatulapo chikhulupiliro mwa imfa ikudza ya KRISTU ndi kuukitsidwa kwake chimene chikanawathandiza kuti ayanjanenso ndi MULUNGU.

Poyambirirapenipeni, MULUNGU analitisa Adamu ndi Hava kuposa zolengedwa zonse. IYE anawapatsa ulamuliro pa zinthu

(*Yapitirira patsamba 2*)

<sup>1</sup> Sal. 9:17, Yes. 5:11-15, 33:10-14, 66:24, Mat. 3:12, 5:29, 7:13, 8:11-12, 10:28, 13:38-42, 47-50, 18:6-9, 22:8-13, 25:31, 41-46, Marko 9:42-48, Luka 3:17, 16:19-26, 2 Ates. 1:7-9, 2 Pet. 2:1-9, Yuda 5-7, Chiv. 14:9-11, 19:20, 20:15, 21:8, 27 <sup>2</sup> Chiv. 13:1-8, 14:8-11, 17:1-15, 18:1-8 <sup>3</sup> Gen. 3:1-6, Yes. 14:9-17, Mat. 24:11-12, 24, 2 Akor. 4:3-4, 11:13-15, 2 Ates. 2:3-12, 2 Tim. 3:13, Chiv. 13:1-8, 11-18, 16:13-14, 17:1-2, 8, 18:2-3, 23, 17:8, 19:19-21, 20:1-3, 7-10 <sup>4</sup> Aro. 5:12-21, 1 Akor. 15:20-22 <sup>5</sup> Mat. 20:28, 26:28, Yoh. 1:29, 3:14-17, 6:51, 10:11-18, 11:49-52, Mac. 5:30-31, 20:28, 26:23, Aro. 5:6-11, 1 Akor. 15:3-4, Agal. 1:3-4, 2:20, 4:4-5, Aef. 5:2, 1 Ates. 1:10, 5:9-10, 1 Tim. 2:5-6, Tito 2:13-14, Aheb. 2:9-10

# SATANA WALEPHERA KATATU KONSE KUTI ALANDE MALO A MULUNGU

(Yachokera patsamba 1)

zonse zimene zili m'chilengedwechi, chin-thu chilichonse chamoyo. Lemba la Genesis 1:28 limatiuza kuti MULUNGU anawauza kuti, "Mubalane, ndipo muchulukane, mud-zaze dziko lapansi, ndipo muligonjetse: mulamulire pa nsomba za m'nyanja, ndi pa mbalame za m'mlengalenga, ndi pa zamoyo zonse zakuyenda pa dziko lapansi." Adamu ndi Hava ankayang'anira dziko lonse lapansi ndi zinthu zonse zimene zili m'dzikoli. Pamene Satana anawanyenga, dziko lonse linalowa mu uchimo pansi pa utsogoleri wa mdyerekezi, choncho MULUNGU anakonza zoti awombole dzikoli pakutsika pansi pano monga munthu.<sup>6</sup> MULUNGU anakhala Mwana wa munthu. IYE anadzikanana yekha chifukwa cha ife, mpaka potifera YEKHA pamtanda, kenako IYE anauka n'kubwereranso Kumwamba.<sup>7</sup>

Yohane 3:16 amanena kuti, "Pakuti MULUNGU anakonda dziko lapansi, koteru kuti anapatsa MWANA WAKE wobadwa yekha, kuti yense wakukhulupirira IYE [osati Satana kapena wina wake] asatayike, koma akhale nawo moyo wosatha." Kukhala ndi moyo wosatha ndikotheka pokhapokha ngati KRISTU, amene ndi MULUNGU, Njira, Choonadi, ndi Moyo, atapitiriza mwa inu ngati moyo wanu (Yohane 14:6).<sup>8</sup> Sikuti mungadzapeze moyo wosatha mukungone na pemphero la anthu ochimwa. Mukuyen-eranso kukhala wophunzira wa Yesu. AM-BUYE anatalamula kuti tizisenza mtanda wathu ndi kumamutsatira IYE (Luka 9:23-25).<sup>9</sup> Kuti tidzalandire moyo wosatha, siti-kufunika kuwusiya mtanda.<sup>10</sup> M'mawu ena, tisamachitenso machimo.

Satana ndi mdani yemwe wagonjetsedwa.<sup>11</sup> Poyamba, zinkaoneka ngati Satana adzalamulira dzikoli kwa tuyaya. Koma masiku ano, tikamvera KRISTU ndi kumukana Satana, boma lake limodzi lolamulira dziko lonse ngakhalenso, matchalitchi ake aupandu omwe amatsogoleredwa ndi Vatican, ufumu udzakhala wathu mwa KRISTU.<sup>12</sup>

Nthawi yachiwiri imene munthu anayesera kuti alande malo a MULUNGU ndiponso ufumu WAKE Kumwamba inali

11:1-9 amatiuza kuti "Ndipo dziko lonse lapansi linali la chinenedwe chimodzi ndi chiyankhulidwe chimodzi. Ndipo zinachitika, pamene anayendayenda paulendo kuchokera kummaŵa, anapeza chigwa m'dziko la Sinara; ndipo anakhala kumeneko. Ndipo ananena wina ndi wina, Tiyeni, tipange njerwa, ndipo tiziotche. Ndipo anali ndi njerwa za miyala, ndi kattondo kuphatikiza. Ndipo anati, Tiyeni, tidzimangire mzinda ndi nsanja, imene pamwamba pake pakafikire Kumwamba; ndipo tidzipangire ife tokha dzina, kuti tisabalalikane kupita kumaiko ena pa dziko lonse lapansi. Ndipo AMBUYE anatsika kudzaona mzinda ndi nsanja, imene ana-manga ana a anthu.

"Ndipo AMBUYE anati, Taonani, anthu ali amodzi, ndipo onse ali nacho chinenedwe chawo chimodzi; ndipo ichi ayamba kuchita: ndipo tsopano palibe chinthu choletsedwa kwa iwo, chimene afuna kuchita. Tiyeni, TONSE tipite, tikasokoneze chinenedwe chawo, kuti aliyense asakamve chinenedwe cha mnzake [monga mmene zilili masiku ano kuti anthu a *Demokalase samamvana* ndi anthu a *Ripabuliki*, koteru palibe chomwe chikuyenda]. Ndipo AMBUYE anabalalitsa iwo pa dziko lonse lapansi: ndipo anapita kukapitiriza kumanga mzinda. Chifukwa chake anatcha dzina lake Babele; pakuti AMBUYE anasokoneza kumeneko chinenedwe cha dziko lonse lapansi; kuyambira pamene AMBUYE anabalalitsa iwo pa dziko lonse lapansi."

Panopa ndi nthawi yachitatu ndiponso yomaliza imene Satana akuyesera kuti alande udindo wa MULUNGU ndi ufumu WAKE. Anthu ena amanena kuti zinthu zosadziwiwa bwino zotchedwa ma *UFO* zimene akuziona ndi zochokera kumapulaneti ena koma limeneli ndi bodza: zimachokera Kumwamba. Ndikudziwa zimenezi chifukwa ndikukumbukira zimene zinachitika nthawi ina ine ndi Susie tili paulendo wopita ku Las Vegas kuti tikamangitse ukwati wathu, kunja kunali kutada ndipo tinali mumsewu waukulu chapakatikati pa Los Angeles ndi Las Vegas. Kunali kutada

nthawi inayake ku Babulo. Apanso zi-nalephera, zachidziwikire. Genesis

pamene Susie, yemwe anali akuyendetsa galimoto, anandigwira dzanja lamanzere n'kundiua kuti, "Tony, tiye tipemphere kwa MULUNGU panopa ndipo timupemphre IYE kuti ngati kulidi zinthu zodabwitsa zotchedwa ma *UFO*, ifeyo tizione." Ndizachidziwikire kuti zinthu zochokera kumapulaneti ena sizingamve pemphero lathu lopita kwa MULUNGU, ndiponso sizingatthe kuyankha pemphero limene timapititsa kwa MULUNGU. Titangomala kupemphera, ma *UFO* ambirimbi anaulukira pa galasi lakutsogolo kwa galimoto yathu. Anafika pafupi kwambiri moti ndinkaganiza kuti atiomba. MULUNGU anayankha pemphero lathu nthawi yomwego. Pamene MULUNGU atangoyankha pemphero lathu nthawi yomwego, chikhulupiro changa mwa MULUNGU ndi kuyankha mapemphero kwa IYE chinalimbitsika koposa.

Zinthu zouluka zimenezi zokhala ngati mateyala zimatchulidwa kambirimbi mu Baibulo.<sup>13</sup> Zinthu zimenezi ndi Angelo odalirika achitetetezo a MULUNGU amene amakhala akufufuza zoipa zimene zikuchitika masiku ano MULUNGU asanathetse zoipa zimene zikuchitika padziko lapansili KRISTU akadzabweranso. MULUNGU amatumiza Angelo m'nthawi yovutayi (chifukwa tikukumana ndi mavuto). Angelo amakapereka lipoti kwa MULUNGU lokhudza zimene aona, ndipo MULUNGUYO amatumiza Angelo owononga kuti akawononge malo ena oipa padziko lapansi.<sup>14</sup> IYE amawononga ndi miliri (amene ali matenda), njala, madzi osefukira, zivomerezi, mvula ya m'kuntho, ndiponso zinthu zina zambiri.

Anthu ambiri ndithu padziko lapansili amakhulupirira kuti anthu adzafika popusitsa MULUNGU. Iwo amaiwala kuti m'mbuyomu, MULUNGU analepheret-sapo mapulani awo. Satana anauza Hava kuti kufa simudzafayi, koma "mudzafanana ndi mulungu." Komatu limeneli linali bodza la mkunkhuniza. Tikutero chifukwa Hava ndi mwamuna wake anamwalira. Komanso, Nimrode pamodzi ndi anthu a m'nthawi yake analephera kumaliza kumanga nsanja, ngakhalenso mzinda sanamange Kumwamba. Zimene ankafunazo sizinatheke ngakhale pang'ono.

Ndiponso, anthu ambirimbi padzikoli awononga ndalamala zamadollar zokwana

<sup>6</sup> Yoh. 1:4-13, 12:46, Aro. 5:6-21, Gal. 4:4-5, Aheb. 2:14-18    <sup>7</sup> Mat. 16:21, 20:17-19, 26:31-57, 28:1-10, 16-20, Marko 10:32-34, Luka 9:23, Yoh. 10:7-18, Mac. 1:1-11, Gal. 2:20, Afil. 2:5-11, Aheb. 12:1-3, 1 Yoh. 3:16    <sup>8</sup> Ezeq. 36:27, Yoh. 14:15-20, 23, 26, 15:3-7, 17:21-23, 26, Aro. 8:10-11, 12:1-2, 1 Akor. 3:9, 16-17, 2 Akor. 6:16-18, Gal. 2:20, Aef. 2:10-22, 3:16-21, Afil. 2:13, Akol. 1:27-29, 2 Tim. 1:14, 1 Yoh. 3:24, 4:4, Chiv. 3:19-21    <sup>9</sup> Mat. 16:24-26, Marko 10:17-30, Luka 9:59-62, 14:26-27, 33, Yoh. 12:24-26, Aro. 8:1-14, 35-37, 12:1-2, 1 Akor. 9:26-27, 2 Akor. 5:9-21, 6:1-10, Gal. 5:16-17, 24, Afil. 3:7-9, Akol. 3:5-17, 2 Tim. 2:4, Tito 2:12, Aheb. 11:8-26, 1 Pet. 4:1-2, Chiv. 12:10-11    <sup>10</sup> Mat. 10:22, 24:13, Mac. 14:22, Aro. 11:22, Akol. 1:22-23, 1 Tim. 4:16, 2 Tim. 2:1-3, 3:13-17, 4:5, Yak. 2:17-26, 5:10-11, 1 Yoh. 2:24-25    <sup>11</sup> Yes. 14: 9-20, Ezeq. 28:11-19, Yoh. 12:31, 2 Ates. 2:3-10, Aheb. 2:14, 1 Yoh. 2:13-14, 3:8, 4:4, Chiv. 1:18, 12:3-4, 9-12, 20:1-3, 7-10    <sup>12</sup> 2 Akor. 6:14-18, Chiv. 18:1-5    <sup>13</sup> Sal. 68:17, Ezeq. 1:1-24, 3:12-13, chap. 10, 11:14-25, Dan. 7:7-9    <sup>14</sup> Gen. 19:1-25, 2 Sam. 24:1-17, 2 Maf. 19:35, 2 Mb. 32:19-22, Sal. 78:49, Mat. 13:41-42, Mac. 12:23, 2 Ates. 1:7-9, Chiv. chap. 8, 9:1-5, 13-15, 14:8-11, 15-20, 15:1, chap. 16, 18:1-2, 21, 19:17-21, 20:1-3, 21:9

mabiliyonu ankhaninkhani, ndipo akufunitsabe kuwononga ndalamu zamadolal matrillion ambirimbiri ena, pofuna kuyesa kusamutsa anthu padziko lapansili kuti akawasiye kupulaneti ina, pulaneti ina imene akukhulupirira kuti ndi yofanana ndi dziko lapansili. Koma zonna zake n'zakuti palibe pulaneti yofanana ndendende ndi dziko lathu lapansili. Dziko lopusitsidwa likudikira mwa dyokodyoko kuti zopusazi zichitike. Iwo akukhulupirira mabodza a boma limodzi limene likulamulira dziko lonse pamodzi ndi tchalitchi chake chochimwa, zomwe zikutsogoleredwa ndi Satana, yemwe MULUNGU ananena kuti adzasocheretsa dziko lonse lapansi m'masiku otsiriza ano (Chivumbulutso 12:9). MULUNGU ananena kuti tchalitchi cha Satana padzikoli, chomwe chimayendetsano zinthu m'boma la Satana lomwe likulamulira dziko lonse, chidzakhazika mumzinda wa mapiri 7 (zimenezi zikuimira Rome, Vatican, ndi bungwe la United Nations).<sup>15</sup> Ngati simukudziwa kuti Vatican ndiye mzindawo, mungopita kukampani yoona za maulendo ndipo mukanene zoti mukufuna kugula tikiti yandege yopita kumzinda wa mapiri 7. Iwo adzakugulitsani matikiti opita ku Rome, m'dziko la Italy. Ndiponso, Rome ameneyu ndi yemwewu amene amayendetsa zinthu mwausatana m'bungwe lija la U.N., lomwe ndi boma limodzi limene likulamulira dziko lonse. Mzinda umenewu unmatchedwanco "Dongosolo la Dziko la Tsopano" ndiponso "mpando wa Satana" (Chivumbulutso 2:13). MAWU A MULUNGU, kudzera mwa Mngelo yemwe ali ndi miliri 7 pamodzi ndi Angelo ena, posachedwapa awononga dziko lapansili (pamodzi ndi anthu onse oipa).<sup>16</sup>

Chivumbulutso 17:1-6, 8 amati, "Ndipo anadza mmodzi mwa angelo asanu ndi awiri akukhala nazo mbale zisanu ndi ziwiri [mbale zimenezi zili zodzadza ndi miliri 7 yomaliza ndipo zanyamulidwa ndi ma UFO, omwe kwenikweni ndi ma IFO, zouluwa zodziwika bwino. Munthu angathe kudziwa bwino ma UFO ngati atadziwa MULUNGU ndiponso MAWU AKE. MULUNGU ndi MAWU (Yohane 1:1, Chi-

**15** Dan. 2:40, 7:19-25, Chiv. 13:1-8, 14:8, chap. 17 ndi 18 **16** Chiv. 8:7-12, 9:1-11, 15, 14:14-20, 16:2-4, 8-12, 17-21



**MAUTUMIKI A ALAMO PA INTANETI**  
[www.alamoministries.com](http://www.alamoministries.com)

vumbulutso 19:13].], nayankhula ndi ine [Mngelo ameneyu anayankhula ndi ine, Yohane], nanena, Idza kuno, ndidzakuonetsa chiweruzo cha mkazi wachigololo wamkulu [Tchalitchi cha Roma Katolika, ndi likulu lake ku Vatican], wakukhala pa madzi ambari [anthu a mitundu yonse padziko lapansi]; amene mafumu a dziko [atsogoleri onse a mayiko, kuphatikizapo oweruza milandu a ku Vatican] anachita chigololo asali pabanja [tchimo lililonse loipa kwambiri ndiponso kuimba mlandu ndi kuimba mlandu anthu osalakwa (anthu a MULUNGU)], ndipo iwo akukhala padziko anawaledzeretsa ndi vinyo wa chigololo chake chochita asali pabanja. [Zimene zikutanthauza zomwe amati kukonza zinthu pa ndale (monga kuvomereza maukwati a amuma kapena akazi okhaokha), kudana kwambiri ndi Ayuda, kudana kwambiri ndi Akhristu, ludzu lofuna magazi kwambiri, kupha anthu, kuba, ndi zinthu zina zambiri zosagwirizana ndi MULUNGU ndiponso MAWU AKE.]

"Ndipo ananditenga [Yohane] kunka nane kuchipululu [dziko lapansi], mu MZIMU; ndipo ndinaona mkazi atakhala pachirombo chofiirtsia [mkazi ameneyu ndi Vatican, chipembedzo chimene chikulamulira dziko lonse, ndipo chirombo chofiarcha ndi bungwe la U.N., lomwe lili galimoto la Vatican. Bungweli limapititsa Vatican ku malo osiyanasiyana pakuti amatha kuwononga ntchito komanso anthu a MULUNGU ndi malamulo ake opondereza. Iye ali ndi], maina ambiri amwano [mwachitsanzo, munthu wina woipa akakhumudwa ndi MAWU a MULUNGU, a ku Vatican pamodzi ndi boma lolamulira dziko lonse amati ndikulakwa kutchula MULUNGU m'masukulu a boma, m'makhoti, pamisonkhano ya ndale, pamiyambo yosiyanasiyana, ndiponso m'malo osiyanasiyana padzikoli. Ndipo popeza anthu ambiri a maudindo mu Tchalitchi cha Roma Katolika amagonana amuna kapena akazi okha-

(Yapitirira patsamba 4)

## Kenya

### Kwa Alamo Ministries,

Landirani moni wathu m'dzina la Yesu Ambuye wathu. Ndikukhulupirira kuti zinthu zikukuyenderani bwino mu utumiki wanu. Tikufuna kuthokoza utumiki wanu chifukwa chotumizira mabuku ndiponso pemphero. Ichi chinalandilidwa kopambana m'tchalitchi mwathu komanso ndi anthu a m'dera lathu. Anthu ambiri asintha miyoyo yaho ndipo alandira Yesu kuhala Mpulumutsi wa miyoyo yaho. Zoonadi mabuku a Alamo amakhala ndi uthenga woona chifukwa tikawagawira ena, anthu ambiri akumatembuzika. Kotero, izi zikutanthauza kuti amakhala ndi uthenga wauzimu wochokera kwa Ambuye (ndi zodzozedwa).

Choncho, abale, taganiza kuti tifalitse uthenga m'midzi yonse komanso m'matchalitchi onse chifukwa mukudziwa bwino lomwe ku Africa kuno anthu ambiri amatsatirabe miyambo ya makolo. Panopa tilipo anthu pafupifupi 20 amene tinaitanidwa ndikutha kulumikizana ndi anthu ena komanso kugawa mabuku ndi nkhani zimene mumalembazi moyenelera. Kotero, timachititsa mapemphero bwinobwino, ndipo tikuyembekezerabe zomwe munatatumizira.

Ponena za M'busa Alamo, ndikukhulupirira kuti posached-

wapa atulutsidwa m'ndende. Ndipo tonse monga gulu tikupemphera ndi kusala kudya. Ndipo ambuye sadzatisiya tokha komanso Baibulo limati, monga pa Salmo 34:18-19, "Yehova ali pafupi ndi iwo a mtima wosweka; apulumutsa iwo a mzimu wolapadi. Masautso a wolungama mtima achuluka: Koma Yehova amlanditsa mwa onsewa." Nkhondoyi si yathu koma ya Ambuye. Werengani Afilipi 4:4-9.

Mulungu akudalitseni.  
Ndine wanu mokhulupilika,  
M'busa Moses Kwemboi  
Endebess, Kenya



M'busa Moses Kwemboi ndi ena mwa anthu a mumpingo mwake akugawa mabuku opindulitsa mumoyo wauzimu olembedwa ndi M'busa Alamo ku Endebess, Kenya.

## SATANA WALEPHERA KATATU KONSE KUTI ALANDE MALO A MULUNGU

(Yachokera patsamba 3)

okha, iwo apanga lamulo latsopano, lonena kuti munthu amene akudana ndi zoti amuna kapena akazi azigonana okhaokha wachita tchimo lalikulu (mlandu wodana ndi munthu). Kukhala ndi maganizo amenewa, ndiye kuti uli ndi Chizindikiro cha Chirombo pamphumi pakos (Chivumbulutso 14:9-11). Zimenezitu n'zoipa kwambiri.], chakukhala nayo mitu isanu ndi iñiri ndi nyanga khumi [zimenezi zikusonyeza kuti boma limodzi lolamulira dziko lonsen lapan-gidwa ndi maboma ambirimbiri, ogwirizana ngati amodzi. Onse amaganiza mofanova; onse amangovomereza chilichonse chimene Satana wanena (Chivumbulutso 17:12-15). Satana amachititsa anthu kuganiza kuti akamavomereza chilichonse chimene iye akufuna, ndiye kuti anthuwo ali ndi mtima wokonda kwambiri dziko lawo ndipo anthu amene amakana zimene Satanayo amafuna amaonedwa ngati osafunira zabwino dziko lawo].

"Ndipo mkazi anavala chibakuwa, ndi mlangali [imeneyi ndi mitundu imene a chipembedzo chaupanduchi cha Roma Katolika chimavala], nakometsedwa ndi golidi ndi miyala ya mtengo wake ndi ngale [ndalamu zonse zimene bungwe lotolera misonkho la Internal Revenue Service limatolera zimapita ku Vatican mosayenelera. A ku Vatican ali ndi ndalamu migolomigolo ya matrillion a madollar ogwiritsira ntchito.]; nakhala nacho m'dzanja lake chikho chagolidi chodzala ndi zonyansitsa, ndi zodetsa za chigololo chake chochita asali pabanja: [Vatican, imene ilinso mpando wa Satana, ndi umboni okwanira wa gweru la tchimo lililonse limene limachitika m'dzikoli, ndi malo ena obisika kwa anthu.] Ndipo pamphumi pake padalembedwa dzina, CHINSINSI, BABULO WAUKULU, MAI WA ACHIGOLOLO NDI ZONYAN-SITSA ZA DZIKO LAPANSI [mawu akuti 'pamphumi pake panalembedwa' akun-

zonse zau Satana].

"Ndipo ndinaona mkazi woledzera ndi mwazi wa oyera mtima [Vatican ya Satana ndiyodziwika bwino pa nkhani yopha anthu padzik, kuphatikizapo kuchotsa mimba, kupha Ayuda ambirimbiri pa nthawi ya ulamuliro wa Nazi (holocaust), khoti la Chiroma lofufuza maganizo a anthu a zipembedzo zina ku Spain, ndiponson kuyambitsa nkhondo zonse zimene zinachitika padzik lapansi], ndi mwazi wa mboni zofera dzina la YESU [Mngelo wa AMBUYE anamuza zimenezi Yohane]; ndipo nditamuona iye [Vatican],... ndipo adzazizwa iwo akukhala padzik, amene maina awo sanalembedwe m'bukhu la moyo chiyambire makhazikidwe a dziko lapansi, pamene anaona chirombo chimene chinaliko, ndipo kubile, ndipo chidzakhalako." "Chirombo chimene chinaliko" chikuimira Rome asanawonongeke, ndipo masiku ano Satana wadzutsanso Rome ndi mzymu wake wausatana, zimene zili gwero la ena mwa mavuto.

Ndikamafotoza za mazunzo amene tchalitchi changa chakumana nawo pa zaka 50 zapitazi, sikuti ndimakhala ndikudandaula kapena kufuna zoti anthu andimvere chisoni, koma ndimafuna kuti aliyense wakuchita izi aone yekha kuti n'zosavuta kupirira zoipa zonse zochokera ku chipembedzo chaupandu cha Roma Katolika, chifukwa MULUNGU wandipatsa vumbulutso. Popanda vumbulutso anthu amwonongeka (Miyambo 29:18). Tizikondwera tikamazunzidwa chifukwa cha YESU. Pangafunike mavolyumu ambiri kuti ndikufotokozereni ena mwa mazunzo amene ndakumana nawo. MULUNGU waniyuza kuti ndikufunika kukhala wolimba



M'bale Solman Raju Kola ndi gulu la alaliki anzake akugawa mabuku olembewda ndi M'busa Alamo m'madera a kumidzi ku Andhra Pradesh, India.

gotanthauza kuti maganizo ake onse amila mu zoipa

mwauzimu ka 100 miliyoni kuposa kulimba kwa chimtengo chachikulu cha oak chomwe chinagwa panja pa tchalitchi changa patanggopita maminitsi 15 nditauza mpingo zimene AMBUYE anandiua.<sup>17</sup> "Odala inu, pamene anthu ada inu, nadzapatula inu, nadzatonza inu, nadzalitaya na wa munthu. Kondwerani tsiku lomweli, tumphani ndi chimwemwe; pakuti, onani, mphotho yanu ndiyayikulu Kumwamba; pakuti makolo awo anawachitira aneneri zonga zomwezo" (Luka 6:22-23).

Ndikukuuzani pamaso pa MULUNGU ndiponson pamaso pa anthu onse a padzik lapansi kuti zimene anthu amazitchula kuti

<sup>17</sup> Read "The Tree," Vol. 6500, "The Most Powerful Position in the Whole Universe," Vol. 19700

(Yapitirira patsamba 8)

### India

Wokondedwa M'bale mwa Kristu,

Mulungu akudalitseni pamodzi ndi mpingo wonse mwa Kristu umene mutukumikira nawo. N'zosangalatsa kuna ntchito zazikulu zimene Mulungu wakhala akuchita kudzera munkhani ndi mabuku anu a Uthenga Wabwino.

Mwachisomo cha Mulungu, mothandidzidwa ndi mpingo wathu, lero tinali m'mudzi wina wotchedwa Dondapudi womwe tinakalalikirako Uthenga Wabwino. Ulendo wathu (wa makilonita 40) unali wapamadzi pabwato, ndipo tinalipo mamembala 36. Mulungu wachita zintchito zazikulu m'katu mwa dera la anthu a Chihindu kudzera m'mabuku anu. Tikukhulupirira kuti anthu ambiri omwe ali osochera apulumutsidwa akawerenga mabuku amenewa m'derali.

Ndikufuna nditumize zithunzi zathu kuti muone mmene ntchito ikuyendera kuno.

Tikupempherera m'bale wathu Tony kuti akhale ndi thanzi labwino komanso kuti atulutsidwe msanga mundende.

Ndine m'bale wanu mwa Kristu, Solman Raju Kola Andhra Pradesh, India



# Umboni wa Scott Durning

Pamene ndinali ndi zaka 11 kapena 12, ndinakumana ndi zoopsa kwambiri zomwe sindingathe kufotokoza zokhudza mizimu yopia. Patapita zaka zingapo, ndinabwera ku Los Angeles ndipo ndinayamba kugwiritsa ntchito mankhwala ozunguza bongo. Izi zinachititsa kuti mutu wanga usamayende bwino ndithu kwa zaka zingapo. Ndinkangoona ngati zinthu sizidzasintha. Ndinkakhulupirira kuti ndine munthu wakufa, ndipo ndinkangokhalira kugwiritsa ntchito mankhwala ozunguza bongo.

Koma tsiku lina, mwachifundo cha Mulungu, ndinkaonera TV m'nyumba ya mnzanga winawake. Kenako ndinaboweka nayo ndipo ndinangoizimtsa. Nditayang'ana panja pa zenera la nyumba yosanja katatu, ndinaona masomphenya ochokera kwa Mulungu. M'masomphenyawo ndinkadziona ine mwini ndili ndi zaka 11, nditaima pakapinga kutsogolo kwa nyumba ina ku Cleveland, Ohio (kumene ndimachokera). Zinthu zinkachitika mofulu-

mira kwambiri m'masomphanyawo moti kwa masekondi 10 okha, ndinakula n'kufika pa msinkhu umene ndiliwu, ndipo ndinali nditaima kutsogolo kwa nyumba yoyandikana nayo. Pamene ndimati ndiziganizira tanthauzo la zinthu zimenezi, Mulungu anayankhula nane. Mulungu anati, "Mulungu analenga dzuwa; Mulungu analenga mwezi; Mulungu analenga dziko; Mulungu analenga nyenyezi; Mulungu analenga udzu; ndipo Mulungu amakulitsa udzuwo." Ndinadabwa kwambiri. Ndiyeno ndinawula kuti, "Dzuwa lake ndi lomweli; dziko lake ndi lomweli; ineyo ndine ndemwe. Ndinangokula ndikuzungulira mutu."

Kungoyambira nthawi imeneyi, moyo wanga unasinthiratu. Ndinkapita kukayenda m'misewu usiku ndikumayankhula ndi Mulungu. Koma patapita nthawi, Mulungu anandiwopseza kawiri konse kuposa momwe ndimaganizilira chifukwa ndinkapitirizabe kuchimwa. Nditasowa mtengo wogwira, tsi-

ku lina ndinapita kutchalitchi chachiKhristu cha Tony Alamo ku Hollywood, California. Ndinali ndisanapiteko kutchalitchi chime-nechi chifukwa ndinkaona kuti si tchalitchi "chachikulu". Apa n'kuti nthawi ili cha m'ma 11:30 usiku. Pa nthawiyo, Tony Alamo anali m'tchalitchimo. Tony anandiyandikira n'kundiua kuti, "Iwe utsalire konkuno." Choncho ndinatsaliradi. Pampapemphero a usiku wotsatira, Abusa a Tony ndi Susan Alamo analiponso. Tony anapereka umboni wake wonse wokhudza mmene Mulungu anayankhulira naye. Ndinali ndisanamvopo zoti mwazi wa Yesu Kristu ndiwokhawo umene umathandiza kuti machimo akhulukidwe. Ndinayamba kuona kuti ndagwidwa ndi Mzimu Woyer. Anthu 30, kuphatikizapo ineyo, anapulumutsidwa pa usiku umenewu. Kenako ndinalowa m'chipinda chopemphera ndipo ndinalandira Ubatizo wa Mzimu Woyer. Ndinkachita kudzimva kuti tsopano ndafika kwathu. Apa panali pa May 11, 1970.

Patangopita nthawi yoposa chaka ndi theka, ndinalembera kalata M'busa Tony Alamo chifukwa ndinkakumana ndi mavuto. Cham'ma 2 koloko m'banda kucha wa tsiku limeleno m'bale wina anandiua kuti Tony Alamo akufuna kuyankhula nane pafoni. Ndinali ndili m'tchalitchi chathu ku Saugus, California. Ndinatenga foniyo n'kunena kuti, "Halo, ndine Scott." Koma kunali zii, osayankhidwa. Ndinabwerezanzo kuti. "Halo, ndine Scott." Kenako ndinamva mawu a Tony Alamo akundiua kuti "Mulungu analenga dzuwa; Mulungu analenga mwezi; Mulungu analenga dziko; Mulungu analenga nyenyezi; Mulungu analenga udzu; ndipo Mulungu amakulitsa udzuwo." Ndinamva kuti ndazunguliridwa ndi Mzimu Woyer ngati khoma lalikulu. Kenako Tony Alamo anayankhula nane pondilangiza molimbika kwa mphindi pafupifupi 45. Ndinali ndisanauzepo munthu aliyense zoti Mulungu anayankhula nane, ngakhalenso zimene Mulungu anandiuza.

Kwa zaka zambiri tsopano, Mzimu Woyer wakhala ukugwira ntchito mu nkhanikapena kuti mabuku a Uthenga Wabwino amene M'busa Alamo amalemba, komanso m'mauthenga onse opita kumatchalitchi. Tony ndi Susan Alamo amanga "mizinda" m'madera osiyanasiyana m'dzikola la United States kuti anthu amene akutumikira m'tchalitchi azikhalamo. Nkhani za Mauthenga Abwino zimene amalemba zakhala zikutumizidwa m'mayiko 200 osiyanasiyana, pamodzi ndi katundu wina wothandizira anthu. Ndikuthokoza Mulungu chifukwa chondipulumsa ndiponsono chifukwa chondipatsa mwayi wokhala mu Utumiki umenewu.

## Myanmar

Wokondedwa Tony Alamo,

Landirani moni wathu wamafuno abwino kuchokera ku Myanmar mwa Ambuye wathu wakumwamba komanso Mpulumutsi wathu Yesu Kristu. Ndikupemphera mochokera pansi pa mtima kuti zinthu zikuyendereni bwino.

Kuyambira mu 2002 Rod and Staff yatanganidwa kukhanzikitsa tchalitchi, kualikira za chitsitsimutso, kusamala odwala, kuperekha thandizo, maphunziro ndi ntchito zina zachitukuko m'madera athu, mapulogalamu osamalira ana/ana a masiye, ntchito yokonza mabuku ndi kuwagawa pakati pa okhulupirira ndi osakhulupirira omwe chimodzimodzi ku Myanmar. Cholinga chathu n'choti tifikire mitundu ya anthu amene sanafikiridwepo ku Myanmar, ndi kuthandiza osakhulupirira kuti amudziwe Kristu pakuwapatsa nkhan, mabuku, ndima Baibulo, kuphunzitsa anthu Baibulo mwachindunji, kusonkhana m'magulu ang'onoang'ono komanso misonkhano ya utumiki, komanso kumasulira ndi kusindikiza mabuku a Chikhristu. Tikuyesetsa kuti ntchito imeneyi ifikire anthu ambiri n'cholinga choti amudziwe Kristu komanso tiyambitse matchalitchi atsopano.

Ndinalimbiksida ndi kudalitsika nditawerenga bukhu limene munalemba lakuti, *Mesiya Mogwirizana ndi Ulosi wa mu Baibulo*. Kungoyambira nthawi imeneyo, ndinakhalo ndi mtima wofunitsitsa kuti ndilimasulire mu Chibamizi, mu Hakha-Chin, ndiponsono mu Mizo (zinenero za ku Myanmar). Popeza bukhuli ndi labwino kwambiri

komanso lolimbikitsa ndikukhulupirira kuti likhala dalitso lalikulu kwa anthu a mtundu wanga. Ku Myanmar, mabuku a Chikristu ndi osowa kwambiri, ndipo anthu ofuna kufalitsa uthenga wabwino anamasulira mabukuwa ndi kuwasindikiza komanso kuwagawa mwa ulere. Mabuku akuthandiza kwambiri ndipo akupindula ku miyoyo ya anthu. Tinganene kuti ndi anthu anayi okha pa anthu 100 aliwonse omwe ndi okhulupirira, ndipo ambiri mwa anthu a m'derali adakali mumdimma. Tikupemphera kuti anthu ambiri ayambe kutsatira mapazi a Yesu kudzera m'mabuku anu. Ndikukhulupirira koposa kuti ludzu la m'mitimaya yavo lidzathetsedwa. (Mitundu ya anthu ya Hakha-Chin ndi Mizo imakhala m'dera la mapiri m'chigawo chakumadzulo. Ali ndi zinenero zawozawo, ndipo ambiri mwa anthu ameneawa satha kuwerenga Chibamizi. Tisan galala kwambiri ngati mungatutumizire mabuku ambiri kuti tiwaike mu laibulale yathu.

Tikufunitsitsa kuti utumiki wanu ufa likire m'dzikola lonse la Myanmar. Ndife okonzeka kugwira nanu ntchito ya Ambuye limodzi ndipo tikukuitanani kuti mufalitse utumiki wanu ku dziko lathu. Ngati mungapeze nthawi tikukufunitsitsani kuti mubwere kuno ku Myanmar chifukwa cha Ufumu Wake.

Ndikuyembekezera mwachidwi kumva kuchokera kwa inu. Mulungu akudalitseni. Mu utumiki Wake,  
M'busa Bawi H. Thang, Director  
Rod and Staff Ministries  
Yangon, Myanmar

# Papa Francis Wapezeka Wolakwa Pa Milandu Wozembetsa Ana, Kugwiririra, ndiKupha

Lamulungu, July 20, 2014, 7:28

by Judy Byington



Dzulo anthu amene akuyimbidwa milandu Papa Francis Bergoglio, wamkulu wa Jesuit ya Katolika wotchedwa Adolfo Pachon ndi Bisihopu Wamkulu waku Canterbury wotchedwa Justin Welby apezeka olakwa pa milandu yogwilirira, kuzunza anthu, kupha anthu komanso kuzembetsa ana. Oweruza asanu a International Common Law Court of Justice imene ili ku Brussels apezeka kuti akhala akuchita milanduyi posachedwa pompa m'chaka cha 2010. Kungoyambira m'mwezi wa March wathawu, [anthu oposa 48 akhala akuikira umboni](#) kukhotili la ICLCJ pazimene anthu oyimbidwa milanduwa akhala akuchita monga mamembala a Ninth Circle Satanic Child Sacrifice Cult.

Zikumveka kuti gulu lochita za Usatana la Ninth Circle Satanic Cult limapereka nsembe za ana a anthu mumatchalitchi a Roma Katolika ku Montreal, New York, Rome, Scotland, London, Carnarvon Castle ku Wales, komanso kumalo ena amene sanatchulidwe a ku French Chateau m'dziko la Holland. Izi zakhala zikuchitikanso m'matchalitchi a Katolika ku Canada ndiponso m'masukulu ogonera pompo a Anglican Indian omwe ali ku Kamloops, British Columbia ndiponso ku Brantford, Ontario ku Canada. Zimamvekanso kuti gulu lochita za Usatanali la Ninth Circle Satanic Child Sacrifice Cult limagwiritsa ntchito nkhalango za anthu wamba zomwe zili ku US, Canada, France ndi ku Holland pochita "Maphwando Awo Ofufuza Anthu" omwe pamafika anthu olemekezeka ochokera m'madera osiyanasiana padzikolone, kuphatikizapo mabanja achifumu a ku Ulaya. Achichepere a zaka zam'mateen zimamveka kuti amasungidwa ndi magulu achifwamba mamaafia, kenako amawavula, kuwagwiririra, kenako n'kuwapha. Mkulu woimira pa milandu (Chief Prosecutor) anati: "Tchalitchi cha Katolika n'chachikulu kwambiri padzikolone koma zikuoneka tchalitchichi chikugwirizana ndi magulu achifwamba mamaafia, boma, apolisi komanso makhoti padzikolone."

Atsikana awiri anauza khoti la ICLCJ kuti Papa Francis anawagwilirira pa nthawi imene ankachita mwambo wopereka

ana nsembe. Anthu enanso okwana 8 anaikira umboni kuti iwo wo anagwiliridwa kapena anaona anthu ena akugwiliridwa komanso anaona ana akuperekedwa nsembe ndi akuluakulu a tchalitchi. Zikumveka kuti gulu lochita za Usatana la Ninth Circle Satanic Cult linachita mwambo wake wopereka nsembe ana nthawi ya dzinja m'chaka cha 2009 ndi 2010 m'madera akumidzi m'mayiko a Holland ndi Belgium.

Malinga ndi chikalata chomatidwa bwino chimene chatengedwa kumalo osungira mabuku ku Vatican, zadziwika kuti Papa Francis anapezeka kuti ndi amene ankalimbikitsa miyambo yopereka ana nsembe pa nthawi imene papayu anali wansembe wongogwirizira komanso Bishopu ku Argentina. Chikalata chinanso chomwe chinalembewa pa December 25, 1967, chotchedwa Magisterial Privilege chikusonyeza kuti Papa aliyense amene wangokhala kumene pa udindowu amafunika kuchita nawo miyambo ya gulu lochita za Usatana la Ninth Circle Satanic Cult monga kupereka nsembe makanda, ndi kumwa magazi awo. Zikalata ziwiri zonsezi zinaperekedwa ngati umboni kukhoti la ICLCJ ndi munthu wina waudindo waukulu ndithu ku Vatican komanso munthu wina amene poyamba ankagwirina ntchito ndi Vatican Curia ndipo anasiya.

Mwezi wathawu munthu wofufuza nkhanzi wa Irish Garda Police Force anapereka umboni pamaso pa oweruza 5 ndiponso anthu ena 27 ogwira ntchito kukhotili kuti zizindikiro zimene zinali pamafupa a ana pafupifupi 796 omwe anapezeka muthanki ya zonyansa za kuchimbudzi cha pamalo ena ogona a Sisitere patchalitchi china cha Katolika ku Ireland, zikusonyeza kuti anawo anachita kuphedwa mwamwambo wawo wa nkhanza kwambiri. Mboni inanena kuti akatswiri omwe anayeza mafupawo anatsimikiza zoti mafupa a anawo akusonyeza zoti anawo anachita kuwapha mwa nkhanza kwambiri powapangira zizimba ndikuwapereka nsembe.

[Chikalata chapa BBC](#) chinavumbula zoypa zimene zinhakala zikuchitika kwa zaka 50 zimembetsa ana zochitidwa ndi tchalitchi cha Katolika ku Spain. Pomafika m'zaka za m'ma 1990, tchalitchi chinali chitaba ana oposa 300,000 kuchokera kwa makolo awo. Makolo a anawa ankauzidwa kuti ana awovo amwalira ndipo awaika m'manda mudzenje limodzi. Zikumvekanso kuti tchalitchi cha Katolikachi chinapeza ndalamu zokwana madola 20 biliyonu ponamiza anthu kuti chikutenga anawo kuti chizikawasamalira.

Mboni inanso inanena zoti iyo inalipo pamene Papa Francis ankachita misonkhano yake ndi gulu la nkondo la Junta pa nthawi imene ku Argentina kunali nkondo yoyipa m'zaka za m'ma 1970. Malinga ndi zimene mboniyo inanena, Papa Francis anathandiza kuzembetsa ana 30,000 amene makolo awo anamangidwa pa zifukwaza ndale ndipo sankadziwika komwe ali. Anawo anawatumiza kugulu lochitira nkhanza ana, lomwe ofesi yake ili ku Vatican.

Pulogalamu ina [ya nkhanzi za padera ya pa ABC](#) inati mdyerekezi amakhala ku Vatican. "Zikalata zachinsinsi

zosungidwa ku Vatican zimene zinaonetsedwa m'khoti monga umboni zinasonyezeratu kuti kwa zaka mahandiredi ambirimbiri, akuluakulu a tchalitchichi majesuit akhala akuchita miyambo yopha ana amene anawaba n'kumamwa magazi awo," mkulu woimira milandu (Chief Prosecutor) kukhoti la ICLCJ anenana zimenezi pouza oweruza 5 ochokera m'mayiko osiyanasiyana komanso anthu ena 27 othandizira poweruza milandu kukhotili. "Akuluakulu a tchalitchichi anayamba kuchita zimenezi pokhulupirira kuti magazi a ana osalakwa angathandize kuti pasamakhale zosokoneza zilizonse Papa akakhala pa udindowu ku Rome. Machitidwe amenewa sanangokhala ongofuna kupha anthu ambirimbiri koma linali dongosolo komanso zinali zokhanzikitsidwa m'chikhalidwe chawo. Zimenezi ndi nkhanza zoopsa kwambiri ndipo n'zomvetsa chisoni kuti tchalitchi n'chimene chikuchita zimenezi. Kuyambira cha mu 1773, zimawoneka kuti amapanga ndi a tchalitchi cha Roma Katolika, majesuit komanso Papa aliyense."

Panakonzedwa zoti anthu ena amene akukhudzidwa ndi zankhanza zimene zinaululika kukhoti la ICLCJ afufuzidwe komanso aimbidwe milandu. Pa September 1, 2014, kafukufuku anakhanzikitsidwa kuti ayambe ndipo mutu wake ndi wakuti Komiti Yokhanzikika Yoona za Kuzembetsa Ana Komanso Kuchita Miyambo Yopereka Ana Nsembe. Kuyang'ana mozama pa malamulo kumayembekezereka kutsatira.

Anthu 48 amene anaperekera umboni pa milanduyi anan ena zoti anthu omwe ankachita zankhanzazi ndi a Papa a Katolika, ndipo aPapawa ndi Francis Bergoglio, Yohane Paulo Wachiwiri ndiponso Joseph Ratzinger; Anglican, United Church ya Canada ndi maofisala a tchalitchi cha Katolika kuphatikizapo Makadinala ndi Superior General wa Jesuit ya Katolika Adolfo Pachon; Mfumukazi Elizabeth ya ku United Kingdom ndi Prince Phillip, Justin Welby yemwe ndi bishopu wamkulu wa Anglican ku Canterbury komanso Fulford yemwe ndi mkulu wa oweruza milandu kukhoti lalikulu; ku Netherlands; makadinala ku Holland ndi Belgium ndi anthu a kubanja lachifumu monga Crown Prince Alfrink Bernhard, Mfumu Hendrick, munthu yemwe amayenda ndi Mfumukazi Wilhelmina ya ku Holland, Mfumukazi Beatrix, bambo ake ndiponso a viceroy, Prince Johan Friso ndi mkazi wake Mabel Wisse Smit, nduna zakale, mkulu wa asilikali ku Holland, mlembi wa Raad van State; maofesala aku Canada, Australia, United Kingdom ndiponso asilikaliaku United States ndi maboma kuphatikizapo [CIA ku USA](#), ndi nduna za boma zodziwika bwino, oweruza milandu, andale komanso amalondaaku United States, Belgium, Holland, Canada, Australia, France, Ireland ndiponso United Kingdom.

## Malawi

Wokondedwa M'busa Alamo,

Zikomo potitumizira nkhani yotiunikira zimene tchalitchi cha Roma Katolika chimachita. Nditengerepo mwayi kukudziwitsani zoti anthu ambiri amene alowa mpingo wathu anali a tchalitchi cha Roma Katolika poyamba ndipo iwo atuluka m'tchalitchichi atawerenga nkhani zimene inu mumalemba. Chonde pitirizani kudziwitsa dziko lonse zinthu zimene zikuchitikadi.

Innocent Mtambo

Chitipa, Malawi

Pa July 19, 2014, khoti linapereka chikalata chopatsa mphamuva apolisi kuti akhonza kumanga anthu amene apezeke olakwa pa mlanduwu. Koma malinga ndi chikalata chimene a ITCCS atulutsa dzulo, padakali pano zikalata zimene ndi umboni wa kukhoti sizimatulidwa m'maenvulopo ake. Pa mlandu woyamba umene khoti la ICLCJ linazenga, womwe unafika mu February 2013, khotili linaona zoti ana 50,000 a ku Canadian amene anasowa, anasowetsedwa ndi anthu 40 otchuka m'dzikoli, kuphatikizapo Mfumukazi Elizabeth.

Ana 50,000 anasowa ku Canada makamaka m'masukulu a Katolika ogonera pomwepo. Malo okhalapo manda oika ana ambiri m'dzenje limodzi oposa 34 anapezeka ku ena mwa masukulu 80 ogonera pompovo m'dzikilo lonse la Canada. Kuyambira 2008, Mfumukazi Elizabeth ndi Boma la Canada akhala akukana pempho la ITCCS lofunu kufukula pansi kuti apeze zotsatira kapena zosiyidwa.

Chifukwa chothekera chimene ankakanira sichinali chodabwitsa. October 10, 1964, Mfumukazi Elizabeth ndi Prince Phillip anapezeka olakwa pa mlandu wozembetsa ana 10 a pasukulu yogonapo ku Kamloops yomwe ili ku British Columbia. Kuyambira nthawi imeneyo mpaka pano, makolo a anawo sanaonenso ana awo. Zakuyang'ana mozama malamulo zikuoneka kuti zinachititsa Papa Ratzinger kutula pansi udindo wake. Umboni ochokera ku milandu imeneyo ukhonza kupezeza mu "[Hidden No Longer](#)" ya Kevin Annett.

[Khoti la dziko lonse la ICLCJ](#) lili ndi maofesala owona za bata ndi mtendere (Common Law Peace Officers) oposa 450 ochokera m'mayiko 13, ndipo amagwira ntchitoyi m'magulu 51 amene ali m'madera osiyanasiyana. Ndalamu zinalipo kwa anthu osiyanasiyana amene anali ndi chidwi chokhala m'magulu n'cholinga chothandiza kuwunikira malamulo okhanzikitsa bata ndi mtendere. Ngati mukufuna kulankhula ndi khoti la [ITCCS](#), ICLCJ ku Brussels, kapena makhoti a m'gululi amene ali m'madera ena kapenango kwa anthu amene amagwira ntchito mongodzipereka polimbana ndi m'chitidwe wankhanzawu, tumizani imeloku: [itccscentral@gmail.com](mailto:itccscentral@gmail.com), [hiddenfromhistory1@gmail.com](mailto:hiddenfromhistory1@gmail.com), mungaimbenso foni ku [386-323-5774](tel:386-323-5774) (USA) kapena [250-591-4573](tel:250-591-4573) (Canada).

## Ivory Coast

(Yamasuliridwa kuchokera ku Chifalansa)

Moni wokondedwa M'busa Alamo.

Ine ndine M'busa Goma Gba Lévi. Kuno ku Ivory Coast tinatseka chitseko cha ufumu wa Kumwamba kwa mabanja angapo pachifukwa chakuti anthu onse amene ali pa ukwati wa mitala sadzalowa mu ufumu wa Mulungu.

Nditawerenga nkhani imene munalemba yokhudza mitala, ndi kuiyerekezera ndi zimene Baibulo limanena, ndikuyamba kugwirizana nanu pakubwera mbali yanu. Tsopano ndikuchitsegula chitsekochi kwambiri. Tiku-pempha Mulungu wachifundo kuti atikhululukire.

Komanso, ndikupempha kuti munditumizire buku lofotokoza nkhani imeneyi ndiponso lakuti "Ana Ena a Mariya." Munditumizireko mabuku 10 akuti Mesiya kuti ndipatseko alaliki ena amene ndikuwaphunzitsa.

Ndine m'bale wanu,

M'busa Lévi

Abidjan, Ivory Coast

# SATANA WALEPHERA KATATU KONSE KUTI ALANDE MALO A MULUNGU

(Yachokera patsamba 4)

ma UFO si zinthu zochokera kumapulaneti ena, koma ndi Angelo a Kumwamba. Ndi kutsimikiza ndi mtima wanga pa zimenezi. Amene angakuuzeni zosiyana ndi zimene ndanenazi apusitsidwa ndi Satana, mofanana ndi mmene anapusitsira Hava, anthu a ku Babulo, bungwe la U.N., ndipo adzakupititsani ku Gehena pamodzi nawo. Umunthu sungatenge komanso sudzatenga malo a MULUNGU. Umunthu unalephereka m'mbuyomu, ndipo udzaptirira kulephera.

YESU KRISTU ndi MAWU a MULUNGU. Khulupirirani pa MAWU a MULUNGU (pa YESU KRISTU), ndipo mudzapulumuka (Machitidwe 16:31). Kuti mulandire KRISTU, MAWU A MULUNGU, nenani pemphero ili:

**AMBUYE** wanga komanso MULUNGU wanga, ndichitireni chifundo ndine munthu wochimwa.<sup>18</sup> Ndikukhulupirira kuti YESU KHRISTU ndi MWANA wa MULUNGU wamoyo.<sup>19</sup> Ndimakhulu-piriranso kuti IYE anafera pamtanda ndipo anakhetsa mwazi WAKE wamtengo wapatali ndi cholinga choti machimo anga onse akhululukidwe.<sup>20</sup> Ndikukhulupiriranso kuti MULUNGU anauksitsa YESU kwa akufa pogwiritsa ntchito mphamvu ya MZIMU WOYERA,<sup>21</sup> ndiponso kuti IYE anakhala kudzanja lamanja la MULUNGU ndipo panopa akumva pemphero langa lolapali.<sup>22</sup> Ndikutsegula

zitseko za mtima wanga, ndipo ndikukuyitanani kuti mulowe mumtima mwanga, inu AMBUYE YESU.<sup>23</sup> Tsukani machimo anga ambirimbiri achoke onse mu mwazi wamtengo wapatali umene INU munak-hetsa m'malo mwanga pamtanda wa ku Kavari.<sup>24</sup> Ndikudziwa kuti mundimvera pemphero langali AMBUYE YESU; INU mukhululukira machimo anga ndi kulpulumtsa moyo wanga. Ndikudziwa izi chifukwa MAWU ANU, Baibulo, li-manena zimenezi.<sup>25</sup> MAWU ANU amati INUYO simudzakana kumvetsera pemphero la munthu aliyense, ndipo ine ndili m'gulu la anthu amenewo.<sup>26</sup> Choncho, ndikudziwa kuti INUYO mukundimvetsera pamene ndikupemphera ndipo ndikudziwanso kuti INUYO mundiyankha komanso mundipulumutsa.<sup>27</sup> Ndipo ndikukuthokozani AMBUYE YESU, chifukwa chopulumutsa moyo wanga, ndipo ndisonyeza kuyamikira mwa kuchita zinthu zimene INUYO munalamula komanso kupewa kuchita uchimo.<sup>28</sup>

Pambuyo pa chipulumutso, YESU ananena kuti munthu ayenera kubatizidwa pomizidwa thupi lonse m'madzi, m'dzina la ATATE, ndi la MWANA, ndi la MZIMU WOYERA. Muziphunzira mwakhama Baibulo la *Buku Lopatulika Ndilo Mau a Mulungu*, [King James Version] ndipo muzichita zimene Baibulolo limanena.<sup>30</sup>

AMBUYE akufuna kuti inuyo muzuwa ena za chipulumutso chanu. Mun-

gathe kukhala wofalitsa uthenga wabwino wa Mbusa Tony Alamo. Tizikutumizirani mabuku mwaulere. Imbani foni kapena tumizani imelo kwa ife kuti mudziwe zambiri. Tikukupemphani kuti muwuzeko ena uthengawu.

Ngati mukufuna kuti dziko lipulumsidwe monga m'mene YESU akulamulira, mukufunika kuperekwa chakhumi kwa MULUNGU. MULUNGU anati, "Kodi munthu angabere MULUNGU? Inde, mwandibera kale. Koma akuti, Ife tikumubera bwanji MULUNGU? Mu chakhumi ndi mu zoperekwa. Anthuwo ndi otembereredwa chifukwa akundibera, ngakhale mtundu wonsewu [dziko lonse lapansi]. Bweretsani nonse chakhumi ['chakhumi' ndi gawo limodzi la magawo khumi (10%) ya malipiro anu] m'nhokwe zanga n'cholinga choti pakhale nyama [chakudya cha Uzimu] mu nyumba YANGA [anthu opulumutsidwa] kuti mundiyese, akutero AMBUYE wa MAKAMU, kuti muone ngati sindidzakutseguliranai mazenera a Kumwamba ndi kukukhuthulirani madalitso amene mudzasowa malo owalandirira." Ndipo ndidzadzudzula anthu okudyerani masuku pamutu ndipo sadzawononga zipatso za nthaka yanu; ngakhalenso mphesa wanu sudzalephera kubala zipatso pa nyengo yake m'minda yanu, watero AMBUYE wa MAKAMU. Ndipo mitundu yonse idzakutchani oda-la: chifukwa dziko lanu lidzakhala labwino, watero AMBUYE wa MAKAMU" (Malaki 3:8-12).

<sup>18</sup> Sal. 51:5, Aro. 3:10-12, 23   <sup>19</sup> Mat. 26:63-64, 27:54, Luka 1:30-33, Yoh. 9:35-37, Aro. 1:3-4   <sup>20</sup> Mac. 4:12, 20:28, Aro. 3:25, 1 Yoh. 1:7, Chiv. 5:9   <sup>21</sup> Sal. 16:9-10, Mat. 28:5-7, Marko 16:9, 12, 14, Yoh. 2:19, 21, 10:17-18, 11:25, Mac. 2:24, 3:15, Aro. 8:11, 1 Akor. 15:3-7   <sup>22</sup> Luka 22:69, Mac. 2:25-36, Aheb. 10:12-13   <sup>23</sup> 1 Akor. 3:16, Chiv. 3:20   <sup>24</sup> Aef. 2:13-22, Aheb. 9:22, 13:12, 20-21, 1 Yoh. 1:7, Chiv. 1:5, 7:14   <sup>25</sup> Mat. 26:28, Mac. 2:21, 4:12, Aef. 1:7, Akor. 1:14   <sup>26</sup> Mat. 21:22, Yoh. 6:35, 37-40, Aro. 10:13   <sup>27</sup> Aheb. 11:6   <sup>28</sup> Yoh. 5:14, 8:11, Aro. 6:4, 1 Akor. 15:10, Chiv. 7:14, 22:14   <sup>29</sup> Mat. 28:18-20, Yoh. 3:5, Mac. 2:38, 19:3-5   <sup>30</sup> Deut. 4:29, 13:4, 26:16, Yos. 1:8, 22:5, 2 Tim. 2:15, 3:14-17, Yak. 1:22-25, Chiv. 3:18

*Ngati mukufuna kudziwa zambiri kapena ngati mukufuna mabuku kapenanso nkhanzi zina zimene zimakusangalatsani, tiimbireni foni kapena tilembereni.*

**Tony Alamo, World Pastor, Tony Alamo Christian Ministries Worldwide • P.O. Box 2948, Hollywood, CA 90078**

**Twenty-four hour prayer and information line: (661) 252-5686 • Fax (661) 252-4362**

**www.alamoministries.com • info@alamoministries.com**

*Tony Alamo Christian Ministries Worldwide imalandira anthu onse ndipo imaperekwa zinthu zofunika Kwa onse amene ali ku U.S. amene akufunitsitsadi kuti ayambe kutumikira AMBUYE ndi mtima wawo wonse moyo wawo wonse ndi mphamvu zavo zonse*

**Maservice amachitikira ku New York City lachiwiri lililonse nthawi ya 8 koloko usiku ndi malo ena usiku okhaokha. Chonde imbani (908) 937-5723 kuti mudziwe zambiri. ZAKUDYA ZIMAGAWIDWA PAMAPETO PA MAPEMPHERO ALIWONSE.**

**Funsani buku la M'busa Alamo, lakuti Mesiya, losonyeza KHRISTU kuyambira ku Chipangano Chakale mu maulosi oposa 333.**

**Khalani wogwira ntchito yokolola miyoyo ya anthu pakukhala ogawira mabuku a M'busa Alamo  
Mabuku ndi zinthu zonse zomvetsera n'zaulere, ndipo simulipira ndalamaya yotumizira**

*Ngati wina akukuuzani kuti muperekwa ndalamaya pa zinthu zimenezi, chonde imbani pa (661) 252-5686.*

**M'BUKU ILI MULI CHIKONZERO CHENICHENI CHA CHIPULUMUTSO (Machitidwe 4:12).  
MUSALITAYE, PATSANI ENA KUTI AWERENGE.**

**Anthu amene muli m'mayiko ena, tikukulimbiksani kuti mumasulire n'chinenero chanu mabukuwa. Ngati  
mukusindikizanso bukuli, musaiwale kuika mawu ali m'munsiwa omwe ndi okhudzana ndi zamalamulo:**